


NJIRA YODALIRIKA YA M'MENE MUNGASEFERE MADZI



1

Gwiritsani ntchito botolo la pulasitiki. Dulani pansi pa botololi (Onani chinthunzi). Litembenuzeni kuti mupange ngati fanelo. Ikani thonje (2 inches) kapena kansalu kopyapyala pafupi ndi kamwa la botolo lanu.



2

Phwanyani makala kukhala tiziduswa ting'onoting'ono. Musaphwanye kwambiri kufikira pa phulusa. Tsukani tizidutsa ndi kuika pamwamba pa thonje lanu ngati pa chithunzichi.



3

Ikani thonje kapena kansalu pamwamba pa tiziduswa tanu tamakala anu kuti tiziduswa tikhale malo amodzi.



4

Mutha kugwiritsa ntchito kamwala kakang'ono kuika pamwamba pa thonje lanu lomwe liri pamwamba pa tiziduswa tanu kuti tisayandame.



5

Thirani madzi anu akuda molingana ndi chinthunzichi. Dikirani kuti madzi asefeke. Mukhoza kugwiritsabe ntchito tizidutsa tanu posefera kufikira pamene mwaona kuti madzi sakusefeka mokwanira.



6

Ngakhale kuti madzi anu osefeka angaoneke oyera, amakhalabe ndi tizilombo toipa toyambitsa matenda. Ikani madzi anu m'botolo lotsuka bwino ndi kuika padzuwa kwa tsiku lonse. Kugwiritsa ntchito njira yosefera ya tiziduswa tamakalayi komanso kuika madzi padzuwa tsiku lonse kungakutsimikizireni kuti madzi anu ndi odalirika kumwa.



For more information visit www.waterwellsforafrica.org

Note: See directions for sanitizing the TRUSTED filtered water using either the SODIS method or the chlorine method.